EXAMINATION No.: ________________ SCHOOL:________________

# CENTRAL WEST EDUCATION DIVISION

2026 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION

MOCK EXAMINATIONS

# CHICHEWA

## PAPER II

**Subject Number: M032/II**

**Tuesday, 18 March** **Time Allowed: 2 hours**

**(1:00 - 3:00 pm)**

(Malikisi 90)

**Malangizo**:

- *Pepalali lili ndi magawo anayi*, **A,*B*,*C*** *ndi* ***D.***
- *Yankhani mafunso onse mumagawo* onse.
- *Pepalali lili ndi* ***masamba osindikizidwa okwana khumi ndi anayi***. *Onetsetsani.*
- *Lembani* ***NAMBALA*** *yanu ya mayeso m'mipata yomwe yaperekedwa pamwamba pa tsamba lililonse.*
- *Yankhani* ***mafunso onse*** *pogwiritsa ntchito mipata yoyankhira yomwe yaperekedwa.*
- *Malikisi a funso lililonse ayikidwa pa funsolo.*
- *Perekani pepala lanu kwa oyang'anira mayeso nthawi yake ikakwana.*



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**EXAMINATION No.: ________________ SCHOOL:________________**

## GAWO A: (Malikisi 40)

1. a. Fotokozani momwe mayina ali m’munsiwa adapangiridwira:

(i) mbusa

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)

(ii) mlimi

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)

(iii) njokaluzi

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)

b. Lembani mitundu ya agwirizanitsi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo:

(i) Khasu lomwe linasowa lapezeka.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(ii) Nguwo yobwereka siilimba m’chiuno.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(iii) Mwana wadya bwino phala lero.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(iv) Ndalidya phala la mwana lija m’mawa omwe uno.

______________________________________________ (Malikisi 1)

2. a. Lembani ziganizo ndi mneni “**menya**” mu kachitidwe ka aneni kawochitidwa kotsatiraka ndipo mutseke mzere kunsi kwa aneni a m’kachitidweko.

(i) kawochitidwa m’chibisira

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)

(ii) kawochitidwa poyera

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

(iii) kawochitidwa monyazitsa

______________________________________________

______________________________________________ (Malikisi 2)

b. Tchulani mitundu ya aperekezi omwe atsekedwa mizere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

(i) Iye adabwera pa njinga yobwereka.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(ii) Chikho chili mu mtsuko waukuluwo.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(iii). Pasukulu pano takhalapo kwa zaka zinayi tsopano.

______________________________________________ (Malikisi 1)

(iv) Mwanayu ali ndi nzeru zochuluka kwabasi.

______________________________________________ (Malikisi 1)

3. a. Tchulani ntchito za alumikizi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

i. Jeke ndi Sandifolo amagwirizana kwambiri.

______________________________________________ (Malikisi 1)

ii. Sadakolole zambiri popeza sadathire fetereza.

______________________________________________ (Malikisi 1)

iii. Iye amakonda zovala zitalizitali ndiponso zotaya.

______________________________________________ (Malikisi 1)

iv. Tidavina bwino koma sadatisupe.

______________________________________________ (Malikisi 1)

b. Lembani ziganizo zomwe zikhale ndi mitundu ya mimvekero yotsatirayi ndipo mutseke mzere kunsi kwa mvekerowo.

(i) wamaonekedwe

______________________________________________ (Malikisi 2)

(ii) wamchitidwe

______________________________________________ (Malikisi 2)



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

(iii). wamamvekedwe

_____________________________________________ (Malikisi 2)

4. a. Lembani ziganizo zokhala ndi "**li**" amene akugwira ntchito zotsatirazi ndipo mutseke mzere kunsi kwake.

(i) Kukhala mgwirizanitsi wamchitantchito

_____________________________________________ (Malikisi 2)

(ii) Kukhala mgwirizanitsi wowerengera

_____________________________________________ (Malikisi 2)

b. Tchulani mitundu ya akapandamneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo ndipo mulembe ntchito zawo.

(i) Dzalanyama ndi <u>phiri lotenga mtunda wautali</u>.

_____________________________________________

_____________________________________________ (Malikisi 2)

(ii). <u>Kalanga ine!</u> Ufa uja wathanso.

_____________________________________________

_____________________________________________ (Malikisi 2)

(iii) Ndi bwino <u>kuthandiza anthu omwe ali m'mavuto</u>.

_____________________________________________

_____________________________________________ (Malikisi 2)

**GAWO B: (**Malikisi 20**)**

5. **Kumvetsa nkhani ndi kutambasula Chiyankhulo**

**Werengani nkhani ili m'munsiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

**SAMVA ADAMVA NKHWANGWA ILI M'MUTU**

Bambo Chandiyang'ana amakhaa m'mudzi mwa Mfumu Mvetsetsani. Iwowa anakhala ndi akazi awo, Mayi Mdapirira. Banjali limakhala mosangalala posatengera kuti adali amphemvumdyerakumthiko.



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Bambo Chandiyang'ana adali ambiyang'ambe motero ganyu aliyense amene angapeze chotsatira chake chidali kutchereza khutu kuti amve kuti wapsa kuti. Chomwe chimadulitsa anthu mutu wazizwa ndi chakuti Mayi Mdapirira samatekeseka. Anthu amawathyolera kamtengo. Ambiri ankayankhula kuti adalidi mayi wochoka pa khomo la anthu. Chimene mayiwa amasalitsa ndi chakuti aonetsetse kuti tsiku lililonse ana awo aone choponya m'mimba.

Ngakhale adali achiledzerere, Bambo Chandiyang'ana adali ndi luso losoka mphasa. Anthu samatha phazi pakhomo la bambowa ndi cholinga chodzagula mphasa za Bambo Chandiyang'ana chifukwa zimakhala zotambasuka komanso sizimakhala kabwere mawa ayi. Bambowa ankagulitsa mphasa zawo pa mtengo wongotaya ndipo amanenetsa mwanthabwala zawo kuti sangamachite kupweteka anthu ngati kuti amachita kukagula wina ayi popeza iwo amasoka okha. Pa chifukwa ichi, amanenetsa kuti padalibe zifukwa zokwanira kuti azigulitsa mphasa zawo pa mtengo woboola m'thumba.

Tsiku lina Bambo Chandiyang'ana adapita kukadula bango mu mtsinje omwe udali ku m'mawa kwa mudzi wawo. Mwachizolowezi, adakwanitsa kumanga mtolo waukulu bwino omwe adanyamula phewa lawo, ulendo wakumudzi, atakatula kunyumba mtolo wabango lawolo, adaganiza zopita kukaututa namalingalira kuti tsiku lotsatiralo akalawirire kung'amba bangolo kuti aliyanike ndi cholinga choti liume bwino. Iwo adangoyenda ndi chakhoma kuopa wina angawakoke malaya.

"Tathirani mayi, ife ndalama si nkhani, inu mukudziwanso," adayankhula modzitamandira choncho bambowa.

"Paja mumadziwanso a Chandiyang'ana kuti ine ndimafuna kulandiriratu. Inu ambiyang'ambe, mumavuta mukapapira." Adatero Mayi Nanyoni.
Bambo Chandiyang'ana adatulutsa ndalama yabotolo limodzi, ndikunena mwathamo, "Paja ife ndalama zidatiyanja, ife ndi ndalama ndi chibale chenicheni, tatipatseni tiyambepo kumwa,"



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Atagwetsa botolo lija Bambo Chandiyang'ana adapisapisa m'thumba kufuna kunamiza wogulitsayo kuti ndalama aziiwala.
"Aaa! Chikuchitika ndi chiyani? Ndalama zinali zambiri m'thumbali koma sindikuzipezamo. Aaaa! Ndikukhulupirira ndazisiya pa kama wanga kunyumba. Ndiye paja ife tikayamba sitifuna kulekeza panjira, tandipatseni, 500 ndibweretsa."
Adapitirira kuyankhula Bambo Chandiyang'ana.
Mayi Nanyoni adawapatsa monga momwe adapemphera posadziwa kuti akubzaa ufa. Ataututa Bambo Chandiyang'ana adafika kunyumba kwawo ndipo adayenda molunjika pomwe adasiya mphasa, yomwe adasoka dzulo lake. Iwo adali atapeza kale wogula yemwe adalonjeza kuwapatsa ndalama zokwanira. Ataunguza pomwe adaika mphasa ija adaona kuti pali ntchentche zokhazokha. Nthawi yomweyo Bambo Chandiyang'ana adalunjika akazi awo nawafunsa komwe mphasa idapita.

"Bambo Ngozo, mwafika nthawi yabwino lero, zakhala bwanji? Mudakamatere masiku onse bwenzi zili bwino. Nane ndimalakalaka kucheza ndi wachikondi wanga. Nanga kodi nthawi zonse kumakhumbira anzanga." Adayankhula mwansangala Mayi Mdapirira. Bamboyo adafunsa diso lili pa mtunda, "Mphasa ili kuti?"

"Mphasa ndagulitsa monga mukudziwa pakhomo pano munachoka osasiya kalikonse, ndagula kachimanga ka m'thungwa kuti ndiphikire ana tidathetha ngati makoswewa. Ana asanu ndi atatu mumati nditani nawo kopanda ndi gaga yemwe. Ana akhae ndi njala ngati bamboo awo sadziwa kusoka mphasa," adayankhula mwachidamula mayiyo, osadziwa chomwe a Chandiyang'ana amaganiza, adangozindikira mbama ili pa tsaya.
"Zachibwana sindifuna, munthu wandilonjeza kale ndalama zabwino, komanso mowa ndapapira kale powerengera mphasa imeneyo. Iwe ungamakambe zopanda ndi mchere womwe," adayankha akusisima Mayi Mdapirira. "Kodi anawa ndi andani? Woyenera kuwadyetsa ndani?" Akuluakulu atamva zomwe zidachitikazo adawakumbutsa Bambo Chandiyang'ana ubwino wakulera ndi kubereka ana achiwerengero chabwino.
Bambo Chandiyang'ana adangoti malovu mkamwa ndee, ndikuyamba kupepesa akazi awo komanso akuluakuluwo chifukwa chosamvera malangizo anjira zakulera.



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Adalonjeza zopita kuchipatala pamodzi ndi mkazi wawo ndikukatenga njira zakulera. Kuchokera pomwepo, adayamba kuphunzitsa anthu ena za ubwino wakulera.

**Mafunso:**

a.

(i) Kodi Bambo Chandiyang'ana amakhala kuti?

_______________________________________________ (Malikisi 1)

(ii) N'chiyani chomwe chidadabwitsa anthu ndi banja la Bambo ndi Mayi Chandiyang'ana?

_______________________________________________

_______________________________________________ (Malikisi 2)

(iii) N'chifukwa chiyani banja la Bambo ndi Mayi Chandiyang'ana lidali losauka?

_______________________________________________

_______________________________________________ (Malikisi 2)

(iv) Perekani zifukwa **ziwiri** zomwe anthu amakondera mphasa za Bambo Chandiyang'ana?

1. _______________________________________________ (Malikisi 1)
2. _______________________________________________ (Malikisi 1)

(v) Tsimikizani popereka mfundo **ziwiri** kuti Bambo Chandiyang'ana adali tambwali.

1. _______________________________________________

   _______________________________________________ (Malikisi 2)
2. _______________________________________________

   _______________________________________________ (Malikisi 2)

(vi) N'chifukwa chiyani Bambo Chandiyang'ana adamenya akazi awo?

_______________________________________________

_______________________________________________ (Maliki 1)

(vii) N'chiyani chomwe chidachititsa Mayi Mdapirira kulandira amuna awo mwansangala?

_______________________________________________

_______________________________________________ (Malikisi 2)



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

(viii) Tchulani mfundo **imodzi** yotsimikiza kuti Bambo Chandiyang'ana adazindikira kulakwa kwawo.

________________________________________________________

________________________________________________ (Malikisi 2)

b. Kusanthula chiyankhulo

(i). Perekani matanthauzo a mawu awa:

1. mphemvum'dyerakumthiko

__________________________________________ (Malikisi 1)

2 wochoka kumudzi kwa anthu

__________________________________________ (Malikisi 1)

3 malovu mkamwa ndee

__________________________________________ (Malikisi 1)

(ii) Kuchokera m'nkhaniyi, pezani mawu mu nkhaniyi omwe ndi ofanana m'matanthauzo ndi awa:

1 ataumwa _________________________________ (Malikisi 1)

2 tidabereka ________________________________ (Malikisi 1)

## GAWO C: (Malikisi 15)

## Chifupikitso

6. **werengani nkhani yotsatirayi mosamala. Nkhaniyi ili ndi mawu 161 ndipo muifupikitse ikhale ndi mawu osachepera 52 komanso asapitirire 55**.

### ULIMI WAMAKONO

Anthu amene amadalira kulima kumunda komanso kudimba pa moyo wawo akuyenera kusintha kaganizidwe kawo. Asinthe kaganizidwe pa kathiridwe ka fetereza, mtundu wambewu zoti abzale, kukula kwa munda komanso kuchuluka kwa anthu ogwira ntchito ndi cholinga chakuti zonse zizichitika pa nthawi yake.



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Anthu amene amalimawa akuyenera kuzindikira kuti sangachite bwino polima malo aakulu pamene sanakonzekere matumba okwanira a fetereza. Ndi chinthu chabwino kudziwa kuti pa ekala imodzi ayenera kugulira matumba anayi, okulitsa awiri komanso obereketsa awiri. Anthu azidziwa kuti manyowa a m'khola lang'ombe, lambuzi, lankhuku, komanso ofukulidwa padzala amathandizanso kumasula nthaka yawo kuti mbewu zawo zikule bwino.

Chinthu china chofunika kwambirinso ndi mtundu wambewu. Ndi kofunika kuti azibzala mbewu monga fumba, njovu, kanyani, mbidzi, mkangala ndi mkango osati yamakolo ndi cholinga chakuti azikolola mbewu zosowa nazo kosungira. Akuyenera kusankha mtundu umodzi kapena iwiri yambewu zomwe zingachite bwino mogwirizana ndi kutentha, kuzizira, mvula komanso dothi lakwawoko.

Anthu olimawa atamatsatira zimenezi polima mu nthawi yake, kubzala mbewu zoyenerera ndi kuthira manyowa komanso fetereza atha kumakolola bwino.



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

EXAMINATION No.: ________________ SCHOOL:________________

**GAWO D:** (Malikisi 15)

**Chimasuliro**

7. **Masulirani nkhani yotsatirayi m'Chichewa chomveka bwino**.

**DROUGHT**

Most farmers in our country rely on rainfall for crop production. This is because most of them are smallholder farmers.

The dependency on rainfall can be affected by drought. This is when an area or a country experiences prolonged dry spell.

Prolonged drought can lead to poor harvest. It can also lead to extinction of aquatic animals. Apart from these, it can cause starvation of other animals.

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

**MAFUNSO ATHERA PANO**



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*